22130523

International Baccalaureate®
Baccalauréat International
Bachillerato Internacional

**CHICHEWA A: LITERATURE – STANDARD LEVEL – PAPER 1**
**CHICHEWA A : LITTÉRATURE – NIVEAU MOYEN – ÉPREUVE 1**
**CHICHEWA A: LITERATURA – NIVEL MEDIO – PRUEBA 1**

Wednesday 8 May 2013 (morning)
Mercredi 8 mai 2013 (matin)
Miércoles 8 de mayo de 2013 (mañana)

1 hour 30 minutes / 1 heure 30 minutes / 1 hora 30 minutos

---

INSTRUCTIONS TO CANDIDATES

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Write a guided literary analysis on one passage only. In your answer you must address both of the guiding questions provided.
- The maximum mark for this examination paper is *[20 marks]*.

INSTRUCTIONS DESTINÉES AUX CANDIDATS

- N'ouvrez pas cette épreuve avant d'y être autorisé(e).
- Rédigez une analyse littéraire dirigée d'un seul des passages. Les deux questions d'orientation fournies doivent être traitées dans votre réponse.
- Le nombre maximum de points pour cette épreuve d'examen est *[20 points]*.

INSTRUCCIONES PARA LOS ALUMNOS

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Escriba un análisis literario guiado sobre un solo pasaje. Debe abordar las dos preguntas de orientación en su respuesta.
- La puntuación máxima para esta prueba de examen es *[20 puntos]*.


© International Baccalaureate Organization 2013

*Lembani ndemanga pa nkhani* ***imodzi*** *yokha. Poyankha funsoli mugwiritse ntchito mafunso onse awiri amene aperekedwa.*

**1.**

"Mutatha kuyimba nyimboyi, munabwerera kwanu. Mutafika kwanu kuja munakhala mu gowero lanu ndipo maganizo anu onse anali pa chikwati chanu chija.

Kenaka adafika anyamata anzanu awiri okondana nanu, omwe adafika kudzaona magule omwe anali kuvinidwa usiku umenewo. Anzanuwo adayamba kukuselewulani kuti usiku umenewo simukanatha kugona chifukwa munali ndi maganizo a mawa lake. Mudangoseka.

Tsono anzanu aja adati kunali koyenera kuti mupite ku bala kukamwa mowa kuti mupeze tulo. Mudavomerezana. Mmodzi wa anzanu awiri aja anali ndi galimoto lake lomwe mudakwera popita kubala kuja. Munali kumwabe choncho m'kati mwa usikuwo, padafika mzungu ndi mkazi wake kuchokera ku Zimbabwe ndipo nawonso anali m'galimoto lofanana kwambiri ndithu ndi lija munakwera inu. Adaimitsa pafupi pompo. Naye pamodzi ndi mkazi wake uja adayamba kumwa.

Ulendo wa mzungu ndi mkazi wake uja unali wopita ku Salima. Inu mutamwa mudaledzera kwambiri, ndipo mudawapempha anzanu awiri aja kuti akuloleni mupite kukapumula m'galimoto. Mudatuluka bwino lomwe koma m'malo mokalowa m'galimoto la mnzanu uja mudakalowa m'galimoto la alendo a ku Zimbabwe aja. Sikutitu mudapusa ayi koma magalimotowo adafananadi kwambiri. Tsono pokhala inu phala linali m'maso mudangolowa n'kukhala pampando wa kumbuyo kwa galimoto la mlendo lija, inu zanu phe, kupha tulo.

Nawonso alendo aja pomwe adatauluka m'bala muja sadaganizenso zoti ayang'ane m'mbuyo mwa galimoto lawo lija. Akadavutikiranji poti anali awiri okha. Nanjinso poti nawo analawako pang'ono ndiye udangopsa ulendo wa ku Salima m'kati mwa usiku, inu muli mtulobe m'mbuypo mwa galimoto lawo.

M'kati mwa njira, mutapitirira kale pa Ntcheu kuchokera kuno ku Zomba mudadzuka pang'ono ku tulo, koma poona kuti galimoto linali kuyenda mudangoganiza kuti mudali kupita kunyumba m'galimoto la mnzanu uja. Kenako ku Lilongwe mbweee, kumbandakucha. Eni galimoto podzayang'ana kumbuyo aona inu muli m'tulo, nayamba kudabwa nau. Pamene adakudzutsani nanunso mudadabwa kuti simunali kwanu ku Zomba ayi koma ku Lilongwe.

Mudasweka mtima podziwa kuti patsikulo mudayenera kukhala kumudzi kuyembekezera kukwatitsa ukwati wanu. Kunali kosatheka kuti mubwerere ku Zomba paulendo wa mituna mazana awiri (200km) n'kukaipeza nthawi yokwatitsira ukwati wanu.

Bola mukadakhala ndi ndalama mukadaitanitsa ndege kuti ikuwulutseni mpaka ku Zomba koma popeza ndinu munthu wa maluzi nthawi zonse ndalama simutha kusunga ndiye munkangoti zunguliluzungulilu mu Lilongwe.

Kumudzi kwanu anthu adayamba kukonzeka. Sadadziwe msanga kuti inu mudalowera ku Lilongwe. Flora bwenzi lanu sadadziwe kuti inu mudalowera ku Lilongwe. Flora adakonzeka. Adatchena kulikonzekera tsikulo. Anthu anu adakonzekanso.

Pokwera dzuwa anthu adayamba kukufunafunani. Pamenepo nkuti anthu ena atasonkhana kale kutchalitchi. Inde anthu akwanu posakuonani adangoganiza kuti mudagona kwa Flora. Nayenso Flora ndi anthu ake posakuonani adangoti mwagona kwanu.

Zakudya zinali zitaphikidwa kale. Mbuzi ndi ng'ombe zinali zitaphedwa ndi kuphikidwa kale. Flora anali chikonzekere. Anthu onse anali achikonzekere kukululutirani, koma inali nkhani yonyansa kudera lanu pamene mnzanu wa ku ofesi adatulukira kutchalitchi alikukombera thukuta kudzapereka uthenga wa lamya wanu wonena kuti mwapezeka ku Lilongwe mosayembekezeka chifukwa chakuledzera kwanu."

P P Litete, *Mkwatibwi wokhumudwa* (1965)

(a) Ndi maphunziro anji amene mlembi akufuna kupereka kwa awerengi kudzera mwa anthu a mu nkhaniyi?

(b) Perekani maganizo anu pa za yemwe akufotokoza nkhaniyi (*point of view*) ndi momwe zikuthandizira kuti mutsatire nkhaniyi bwinobwino.

**2.**

**Wandidolola Mtima**

Wandidolola mtima Namwaliwe.
Ndipo ndikakuona, maso
anga amalenguka.
Mtima wanga umachita
chiphidigoliro.
Timilomo tako towala bwino
ngati mpunga
timasuntha wanga moyowu.
Namwaliwe wandidolola
mtima ndithu.
Chifukwa timawu tako
timakhala ngati Salimo
la ulemu mu mtima mwangamu.
Umati ukangomwetulira,
ine nkhongono
zonse zimachita dzazi.

Ukangowonetsa mana ako oyera bwinowo
mtima wanga umakankha mwazi.
Ndipo thupi lonse
limachita tsembwe.
Mkazi iwe wandidolola
mtima mbambadi.

Ndayendayenda m'dziko lonseli
koma wangati iwe sindinampeze.
Ndazungulira m'mayiko ena
njole yofanana ndi iwe sindinaipeze.
Kunena zoona mkazi iwe
wandiswa mtimawu.
Kukongola kwako kwathetsa
mankhalu a mtima wanga.
Wandidolola mtima Namaliwe.

Clement Gama, *Mkwaso newspaper* (2012)

(a) Fotokozani luso la kalembedwe limene mlembi wagwiritsa ntchito mu ndakatuloyi ndipo zotsatira zake ndi zotani kwa wowerenga.

(b) Litilitcha ndi kalilole (galasi loonera) woona za chikhalidwe cha anthu. Malinga ndi momwe mukumvera ndakatuloyi ndi zinthu ziti zomwe zikuyimira maganizo kapena zikhulupiriro za anthu pa za kukongola kwa mkazi.